
مساجدِ مدینہ (CHICHEWA)


# MASĀJID AL-MADINAH











Sheikh-e-Tariqat Amir-Ahl-e-Sunnat Il fondatore di Dawatelslami Allama Moulana Abu Bilal

**MUHAMMAD ILYAS**

**Attar Qadiri Razavi**

Oyambitsa

Lamasulidwa m'chichewa ndi

مساجدِ مدینہ

# Masājid al-Madinah

Kabukuka kanalembedwa mu chiyankhulo cha Urdu Ndi Nthambi Yofufuza Mabuku achisilamu ya Dawat-e-Islami (*Madinat al-ʿIlmiyya*). **Nthambi yomasulira ya (Dawat-e-Islami)** yamasulira mu Chichewa. Ngati mutapeza cholakwika chilichonse pomasulira kapena pa kalembedwe, chonde dziwitsani nthambi yomasulira pa positi kapena imelo adilesi ili m'musiyi ndi cholinga chopeza sawabu.

**Nthambi Yomasulira (Dawat-e-Islami)**

Aalami Manani Markaz, Faizan-e-Madinah, Mahallah Saudagran,
Purani Sabzi Mandi, Bab-ul-Madinah, Karachi, Pakistan

**UAN:** ☎+92-21-111-25-26-92 – Ext. 7213

**Imelo:** 🖃 translation@dawateislami.net

**Masājid al-Madinah**

MAWUMWINI ONSE NDI OTETEZEDWA © 2024 Maktaba-tul-Madinah

Palibe gawo lililonse la bukuli lomwe litha kutulutsidwa, kapena kutumizidwa, m'mawonekedwe aliwonse kapena mwanjira iliyonse, zamagetsi, zamakina, kuchulikitsa, kujambula kapena mwanjira ina iliyonse, popanda chilolezo cholembedwa cha Maktaba-tul-Madinah.

**Kufalitsidwa koyamba:** Dhū al-Qaʿdah - 1446 AH – (July, 2024)
**kumasulidwa ndi:** Nthambi Yomasulira ya (Dawat-e-Islami)
**Wosindikiza:** Maktaba-tul-Madinah
**Kuchuluka:** -

## THANDIZO

Chonde khalani omasuka kulumikizana nafe ngati mukufuna kuthandiza pa kusindikiza kwa buku lililonse lachipembedzo kapena kabuku pofuna kutumiza thawāb kwa anthu omwe anamwalira am'banja mwanu.

**Maktaba-tul-Madinah**

Aalami Manani Markaz, Faizan-e-Madinah Mahallah Saudagran,
Purani Sabzi Mandi, Bab al-Madinah, Karachi, Pakistan

✍ **Imelo:** maktabaglobal@dawateislami.net – maktaba@dawateislami.net
✆ **Foni:** +92-21-34921389-93
💻 **Webusayiti:** www.dawateislami.net

اَلۡحَمۡدُ لِلّٰہِ رَبِّ الۡعٰلَمِیۡنَ وَ الصَّلٰوۃُ وَالسَّلَامُ عَلٰی خَاتَمِ النَّبِیّٖنَ

اَمَّا بَعۡدُ فَاَعُوۡذُ بِاللّٰہِ مِنَ الشَّیۡطٰنِ الرَّجِیۡمِ بِسۡمِ اللّٰہِ الرَّحۡمٰنِ الرَّحِیۡمِ

## *Du'ā*' powerenga buku

Werengani du'ā (pempho) yotsatirayi musanawerenge buku lachipembedzo kapena musanayambe phunziro lachisilamu; mudzakumbukira china chilichonse mwaphunzira komanso mwa werenga اِنۡ شَآءَ اللّٰہ.

اَللّٰهُمَّ افْتَحْ عَلَيْنَا حِكْمَتَكَ وَانْشُرْ

عَلَيْنَا رَحْمَتَكَ يَا ذَا الْجَلَالِ وَالْاِكْرَام

**Kumasulira:**

**E Allah! Titsegulireni makomo a maphunziro komanso a nzeru zakuya, ndipo mutichitire chifundo! E inu amene muli Wawulemerero komanso Wolemekezeka!** ***(Al-Mustaṭraf, vol. 1, p. 40)***

**Chidziwitso:**

Mfunireni zabwino (salat) Mtumiki wokondedwa ﷺ kamodzi kumayambiriro komanso kumapeto kwa Du'a.



www.dawateislami.net

# M’ndandanda wa zopezekamo

Masājid al-Madīnah........................................................................1
Ubwino omufunira zabwino Mtumiki............................................1
Masājid al-Madinah........................................................................2
1. Masjid Qubāˈ ..............................................................................3
Malipiro a umrah ............................................................................3
Al-Fārūq al-Aʿẓam رضی اللہ عنہ ndi Masjid Qubāˈ ..............................3
ʿAbdullāh b. ʿUmar رضی اللہ عنہما ndi Masjid Qubāˈ ............................4
2. Masjid al-Faḍīkh ........................................................................4
3. Khamsah (kapena Sabʿah) Masājid ..............................................5
4. Masjid al-Ghamāmah.....................................................................6
5. Masjid al-Ijābah ..........................................................................7
6. Masjid al-Suqyā............................................................................8
7. Masjid al-Sajdah...........................................................................9
8. Masjid al-Dhūbāb (kapena Masjid al-Rāyah) ..............................10
9. Masjid ʿAynayn ..........................................................................11
10. Masjid Mashrabah Umm Ibrāhīm ...............................................12
11. Masjid Banī Qurayẓah ..............................................................13
12. Masjid al-Nūr ...........................................................................13
13. Masjid al-Fasḥ ..........................................................................14
14. Masjid Banī Ẓafar (kapena Masjid al-Baghlah) .........................15
15. Masjid al-Māˈidah ....................................................................16
16. Masjid Banī Ḥarām....................................................................17
17. Masjid al-Shaykhayn .................................................................19



www.dawateislami.net

18.Masjid al-Mustarāḥ ........................................................ 20
19. Masjid al-Misbah kapena Masjid Banī Unayf ........................... 21
20. Masjid Banī Zurayq ........................................................ 22
21. Masjid Katībah ........................................................ 23
22. Masjid Banī Dīnār ........................................................ 23
23. Masjid al-Mīnāratayn ........................................................ 24
Mbuzi yakufa ........................................................ 25
24. Masjid al-Jumuʿah ........................................................ 26
25. Masjid al-Muʿarrās ........................................................ 26
26. Masjid Dhū al-Ḥulayfah ........................................................ 27
27. Masjid al-Qiblatayn ........................................................ 28



www.dawateislami.net

اَلْحَمْدُ لِلّٰہِ رَبِّ الْعٰلَمِیْنَ وَالصَّلٰوۃُ وَالسَّلَامُ عَلٰی خَاتَمِ النَّبِیّٖن
اَمَّا بَعْدُ فَاَعُوْذُ بِاللّٰہِ مِنَ الشَّیْطٰنِ الرَّجِیْمِ بِسْمِ اللّٰہِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِیْمِ

Zomwe zili m'bukuli zatengedwa kuchokera mu nkhani 130 za omukonda mtumiki: kuphatikizapo Malo Oyera a Makkah ndi Madinah (Tsamba. 237 – 258)

# Masājid al-Madīnah

**Du'a ya Attar:** E Mbuye wowolowa manja! Aliyense angawerenge kapena kumvera kabuku ka masamba 29 kotchedwa *Masājid al-Madinah*, muloleni kuti adzapite malo awiri oyera mwawulemu, ndipo mukhululukireni komanso makolo ake mopanda kufunsidwa zintchito zake.

اٰمِیْن بِجَاہِ خَاتَمِ النَّبِیّٖن صَلَّی اللّٰہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم

## Ubwino omufunira zabwino Mtumiki

Mtumiki wolemekezaka صَلَّی اللّٰہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم anati:

> Lachinayi likafika, Allah Wamphanvu zonse amatumiza angelo ali ndi mipukutu yopangidwa ndi siliki komanso zolembedwa za golide. Amalemba dzina la aliyense amene wandifunira zabwino mochuluka Lachinayi komanso mu usiku wa Lachisanu.[1]

صَلُّوْا عَلَی الْحَبِیْب صَلَّی اللّٰہُ عَلٰی مُحَمَّد

[1] Kanz al-ʿUmmāl, buku. 1, tsamba. 250, hadith 2,174

## Masājid al-Madinah

Muli mizikiti yambiri mkati komanso kuzungulira al-Madinah al-Munawwarah imene ili yolumikizana ndi Mtumiki Wolemekezeka صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم. Yochepa yatchulidwa kuti mupeze manalitso ndicholinga choti anthu opitiko atha kukafufuza mizikiti imeneyi ndikupempheramo pemphero osakakamizika (*nafl*) kulikonse angapeze mizikiti imeneyi. Ndipo komwe sangapeze uliwonse akuyenera kusakasaka ndikupeza mizikiti imeneyi, atha kuwona malo amenewa ndi maso achisoni ndikupeza manalitso. Akuyenera kupempha ma du'a m'mizikiti imeneyi, chifukwa ma du'a amayankhidwa pa malo aliwonse omwe mtumiki wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anafikapo. Shaykh ʿAbd al-Ḥaqq Muḥaddith al-Diḥlawī رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anayankhula momveka bwino ali mu chikhalidwe chakudzipereka kuti:

> Anthu omwe ali ndi uzindikiri wamkati amadziwa kuti kukongola komanso ungwiro wa mtumiki wokondedwa ndi wodala صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم kunawalitsa mapiri komanso zigwa [za Makkah ndi Madinah]. Ndithudi, izi zili chonchi chifukwa Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anayang'ana pa chiduswa china chilichonse cha malo amenewa, kuwalemekeza kuti amuwone iye.[1]

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

[1] Jadhb al-Qulūb, tsamba. 148



www.dawateislami.net

## 1. Masjid Qubāʾ

Pafupifupi makilomita atatu kum'mwera chakumadzulo kwa Madinah al-Munawwarah kuli mudzi wakale wotchedwa Qubāʾ, kumene mzikiti wodalitsika wa Quba ukupezeka. Kupambana kwa mzikiti umenewu kwatchulidwa mu Quran yolemekezeka ndi mu hadith yowona. Munthu atha kufika ku Nzikiti wa Qubāʾ kuchokera ku al-Masjid al-Nabawī (mzikiti wa mtumiki) pafupifupi mu mphindi zokwana 40 poyenda wapansi pa kayendedwe ka pakatikati. Zanenedwa mu *Ṣaḥīḥ al-Bukharī* kuti Mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ankapita ku Masjid Qubāʾ loweruka lililonse, wapansi kapena atakwera chinyama.[1]

### Malipiro a umrah

Kunena kuwiri kwa Mtumiki Opambana صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم:

1. Kupemphera salah mu nzikiti wa Qubāʾ kumafanana ndikupanga umrah imodzi.[2]
2. Amene angapange wudu ku nyumba kwake kenako ndikupita ku nzikiti wa Qubāʾ ndikupemphera salah mmenemo, malipiro ake amakhala ngati a umrah.[3]

### Al-Fārūq al-Aʿẓam رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ ndi Masjid Qubāʾ

Khalifa wachiwiri wa Asilamu Sayyidunā ʿUmar b. al-Khaṭṭāb

---

[1] Ṣaḥīḥ al-Bukhārī, buku. 1, tsamba. 402, hadith 1,193
[2] Sunan al-Tirmidhī, buku. 1, tsamba. 348, hadith 324
[3] Sunan Ibn Mājah, buku. 2, tsamba. 175, hadith 1,412



www.dawateislami.net

رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ analowa mu nzikiti wa Qubāʾ kenako anati:

> Ndikulumbira mwa Allah! Kupemphera salah imodzi mu nzikiti uwu ndikokondedwa kwambiri kwa ineyo kuposa kupemphera salah imodzi mu nzikiti wa Bayt al-Muqaddas ndikuphatikiza ndi ma rakah ena anayi. Zinakakhala kuti mzikiti uwu uli dera lakutali, tinakazitopetsabe ngamila zathu ndi cholinga chokafika ku nzikiti umenewu.[1]

## ʿAbdullāh b. ʿUmar رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُمَا ndi Masjid Qubāʾ

Sayyidunā ʿAbdullāh b. ʿUmar رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُمَا ankapita ku nzikiti wa Qubāʾ loweruka lililonse.[2]

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب          صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## 2. Masjid al-Faḍīkh

Mzikiti uwu ukupezeka pa mtunda wa kilomita imodzi chakum'mawa kuchokera ku Nzikiti wa Qubāʾ. Pamene gulu la nkhondo la chisilamu linazungulira mtundu wa Banū Naḍīr, msasa wa Mtumiki wolemekezeka صَلَّى اللّٰہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم unakhazikitsidwa pamenepa, ndi iye صَلَّى اللّٰہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم anapemphera salah pamenepa kwa masiku okwana 6.[3] Mzikiti umenewu unamangidwa

[1] Kanz al-ʿUmmāl, buku. 7, tsamba. 62, hadith 38,174

[2] Saḥīḥ Muslim, tsamba. 724, hadith 1,399

[3] Wafāʾ al-Wafāʾ, buku. 2, tsamba. 821



www.dawateislami.net

pokumbukira zimenezi. Anthu ena amalakwitsa powutchula kuti Masjid al-Shams.

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِیْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## 3. Khamsah (kapena Sabʿah) Masājid

Kumpoto chakumadzulo kwa Madinah, pafupi ndi phiri la Sela, kuli mizikiti isanu imene ili yoyandikana. Zenizeni zake ndi zakuti, m'mbuyomo panali mizikiti 7 pamalo amenewa. Mu chiyankhulo cha chiarabu, سَبْعَ amatanthauza 7. Choncho, malo amenewa ankatchedwa Sabʿah Masājid. Lero lino mizikiti isanu yokha ndi yomwe inatsala. Muchiarabu, خَمْسَه amatanthawuza 5. Choncho, malo amenewa pang'onopang'ono anatchuka ndi dzina loti Khamsah Masājid. Umodzi mwa mizikiti imeneyi uli pa phiri, umene utha kufikiridwa pogwiritsa ntchito masitepe amene anamangidwa; Nzikiti umenewu umatchedwa Masjid al-Fatḥ. Panthawi ya nkhondo ya chitaganya, Mtumiki wopambana صَلَّى اللّٰه عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anapempha chipambano cha Asilamu pa malo ake amenewa kwa masiku atatu otsatizana: Lolemba, Lachiwiri ndi Lachitatu. Patsiku lachitatu, iye صَلَّى اللّٰه عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anapatsidwa nkhani yabwino ya chipambano pakati pa nthawi ya Ẓuhr ndi ʿAṣr. Ichitu chinali chipambano chotsimikizika moti anthu osakhulupirira anapitirira kukhala ogonjetsedwa/ opanda mphanvu /olamulidwa/wotsekeredwa pambuyo pa chipambanochi.



www.dawateislami.net

Sayyidunā Jābir رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ anati, "Nthawi iliyonse ndakumana ndi vuto, Ndimapita ku Masjid al-Fatḥ ndipo ndimapempha du'a, ndipo mavuto anga amathetsedwa."

Mayina a mizikiti ina 6 kupatula Mzikiti wa al-Fatḥ ndi awa:

1. Masjid Abū Bakr رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ (Kwenikweni ndi Masjid ʿAlī b. Abī Ṭālib رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ).
2. Masjid ʿUmar b. al-Khaṭṭāb رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ.
3. Masjid ʿAlī رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ. Posachedwapa, unkatchedwa Masjid Abu Bakr رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ.
4. Masjid Fāṭimah رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہَا (Mzikiti umenewu kunalibe mu nthawi ya ma sahaba olemekezeka عَلَیْہِمُ الرِّضْوَان. Mbiri yake ikupezeka mu nkhani. Zikunenedwa kuti unamangidwa pambuyo pa chaka cha 1329 pambuyo pa msamuko (1911 C.E.)
5. Masjid Salmān al-Fārisī رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ.
6. Masjid Abū Dharr al-Ghifārī رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ.

صَلُّوْا عَلَی الْحَبِیْب صَلَّی اللّٰہُ عَلٰی مُحَمَّد

## 4. Masjid al-Ghamāmah

Poyenda kuchokera ku Makkah kapena Jeddah kupita ku Madinah, mukhoza kuwona mzikiti wokongola mu njira



www.dawateislami.net

yopita ku al-Masjid al-Nabawī uli ndi zimphika zitalizitali. Umenewu ndi Mzikiti wa al-Ghamāmah. Mu chaka chachiwiri pambuyo pa msambuko, mtumiki wathu wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَالِهٖ وَسَلَّم anapemphera Salah ya Eid al-Fiṭr ndi Eid al-Aḍḥā koyamba pa malo amenewa ndiponso pa bwalo. Komanso, iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَالِهٖ وَسَلَّم anapempherera mvula pa malo amenewa. Nthawi yomweyo, mitambo inabwera, ndipo nvula inayamba kugwa. Liwu la chiarabu la mitambo ndi غَمَامَه, choncho ndi chifukwa chake mzikiti umenewu umatchedwa Masjid al-Ghamāmah. Apatu panali pa bwalo. Sayyiduna ʿUmar b. ʿAbd al-ʿAzīz رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه, amene anatsitsimutsa chisilamu m'zaka za zana loyamba la nsamuko komanso mtsogoleri wa Asilamu, anamanga mzikiti pamenepa.

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## 5. Masjid al-Ijābah

Mzikiti umenewu ndi umodzi mwa mizikiti 9 yakalekale ya ku Madinah. Umapezeka pa Shāriʿ Malik Faisal (kale pamkatchedwa Shāriʿ Sittīn), kumpoto chakum'mawa kwa manda a al-Baqīʿ (kumanzere kwa mphambano ya Shāriʿ Sittīn ndi Shāriʿ Malik ʿAbd al-ʿAzīz). Mtumiki Wolemekezeka صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَالِهٖ وَسَلَّم anapempherako ma rakah awiri a salah pa malo amenewa ndipo anapanga ma du'a atatu; awiri anayankhidwa, pomwe imodzi inaletsedwa. Madu'a atatu ake ndi awa:

1. E Allah! Ummah wanga usadzawonongedwe ndi chilala. (inayankhidwa)

2. E Allah! Ummah wanga usadzawonongedwe ndi kumizidwa. (inayankhidwa)

3. E Allah! Ummah wanga usadzamenyane okhaokha. (Du'a imeneyi inaletsedwa.)[1]

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب    صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## 6. Masjid al-Suqyā

Nzikiti umenewu ukupezeka pafupi ndi nyumba yosungiramo zinthu zakale mkatikati mwa siteshoni ya sitima ya Madinah. Unamangidwa pa malo akale pamene Mtumiki Wopambana صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anapempha du'a kuwapemphera anthu okhala ku Madinah. Mtsogoleri wachinayi wa Chisilamu Sayyidunā ʿAlī al-Murtaḍā رَضِىَ اللهُ عَنْهُ anati:

> Tinanyamuka limodzi ndi Mtumiki wa Allah صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم. Panthawi yomwe tinayandikira Ḥarrat al-Suqyā, amene anali malo a Saʿd b. Abī Waqqāṣ, Mtumiki wa Allah صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anayitanitsa madzi kuti apangire wuzu. Choncho, anapanga wudu, anayima moyang'ana ku Qiblah, ndipo kenako anati [pamene amkawapangira du'a anthu aku Madinah]:

[1] Ṣaḥīḥ Muslim, tsamba. 1544, Hadith 2890



www.dawateislami.net

> "E Allah! Ibrāhīm anali kapolo wanu komanso bwenzi lanu; anawapemphera madalitso anthu aku Makkah. Ndine kapolo wanu komanso Mtumiki wanu; Ndikukupemphani kuti muwapatse anthu aku Madinah madalitso ochuluka muma *mudd awo* komanso *ṣāʿ* [miyeso iwiri] poyerekeza ndi anthu okhala ku Makkah."[1]

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيب صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## 7. Masjid al-Sajdah

Nzikiti umenewu ukupezeka pa malo opatulika pamene nkhani yodziwika inachitikira. Zanenedwa mu buku lotchedwa *Jannat Mayn Lay Jaanay Walay Aʿmaal* (tsamba. 496):

> Sayyiduna ʿAbd al-Raḥmān b. ʿAwf رضی اللہ عنہ anafotokoza kuti nthawi inayake, anamutsatira Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم pamene iye anatuluka. Mtumiki Wolemekezeka صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم analowa m'munda wa tende ndipo anapanga sajidah kwa nthawi yayitali mpakana Sayyidunā ʿAbd al-Raḥmān b. ʿAwf رضی اللہ عنہ anayamba kuchita mantha kuti mwina wamwalira. Choncho, anayandikira ndikuyang'ana mosamala. Mtumiki wolemekezeka صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anadzutsa mutu wake kenako anati, "E ʿAbd al-Raḥmān! Chavuta ndi chani?"

[1] Sunan al-Tirmidhī, buku. 5, tsamba. 482, hadith 3,940



www.dawateislami.net

ʿAbd al-Raḥmān b.ʿAwf رَضِیَ اللّٰہ عَنْهُ anatchula chomwe amkawopa kuti mwina chachitika. Poyankha, Mtumiki Wopambana صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ananena kuti Jibrīl عَلَيْهِ السَّلَام analankhula naye ponena kuti kodi sizinamubweretsere iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم chisangalalo zoti Allah Wamphanvu zonse wanena kuti adzamupatsa madalitso aliyense amene amene wamfunira iye zabwino صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم, komanso zoti adzamuteteza aliyense amene wamfunira iye mtendere صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم.[1]

Pokumbukira zimenezi, Masjid al-Sajdah unamangidwa pamalo amenewa. Nzikiti umenewu unamangidwanso mwatsopano. Ndipo ulipobe, koma uli ndi dzina lina lotchedwa: Masjid Abū Dhar.

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## 8. Masjid al-Dhūbāb (kapena Masjid al-Rāyah)

Popita ku phiri la Uḥud kuchokera ku Thaniyyat al-Wadāʿ, kumanzere komanso kumpoto kwa Madinah, kuli phiri lotchedwa Dhubāb. Pobwelera ku nkhondo ya Tabūk, kapena pa nthawi ya nkhondo ya Khandaq (ngati momwe zikunenedwera mu nkhani zina), hema wa Mtumiki wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم inakhazikitsidwa pa Phiri limeneri.

[1] Musnad Aḥmad, buku. 1, tsamba. 406, hadith 1,662



www.dawateislami.net

Zikunenedwa kuti Mtumiki Woyera صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anapemphera salah pa Phiri la Dhubāb.[1]

Pokumbukira zimenezi, Sayyidunā ʿUmar b. ʿAbd al-ʿAzīz رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anamangitsa nzikiti pa Phiri limeneri. Umatchedwa Masjid Dhubāb kapenanso Masjid al-Rāyah. Kalekale, unkatchedwa Masjid al-Qarīn ndi Masjid al-Zāwiyah.

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## 9. Masjid ʿAynayn

Nzikiti umenewu unamangidwa pa Phiri la al-Rumāh, limene lili loyang'anizana ndi khomo la malo a mpumulo a Sayyidunā Ḥamzah رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ kulowela mbali yaku Qiblah. Patsiku limenelo pomwe nkhondo ya Uḥud imkachitika, asilikali oponya mivi achisilamu anayima pamenepa. Zikunenedwa kuti Sayyidunā Ḥamzah رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ anavulazidwa ndi nkondo pa malo ake omwewa. Sayyidunā Jābir رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ anafotokoza kuti Mtumiki Wopambana صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم, pamodzi ndi masahaba ake عَلَيْهِمُ الرِّضْوَان, anapemphera salah pamenepo ali ndi zida.[2]

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

---

[1] Jadhb al-Qulūb, tsamba. 136-137; Wafāʾ al-Wafāʾ, buku. 2, tsamba. 875

[2] Wafāʾ-ul-Wafāʾ, buku. 2, tsamba. 848-849



www.dawateislami.net

## 10. Masjid Mashrabah Umm Ibrāhīm

Nzikiti wodalitsikawu unamangidwa m'munda wa mitengo ya tende pafupi ndi Ḥarrah Sharqiyyah. Mashrabah amatanthawuza munda, ndipo Umm Ibrāhīm akunena za Mayi Māriyah Qibṭiyah رضی اللہ عنہا, amene anali mwini wake wa munda. Sayyidunā Ibrāhīm رضی اللہ عنہ, amene anali mwana wamamuna wokondedwa wa Mtumiki Woyera صلی اللہ علیہ واٰلہٖ وسلم, anabadwira m'munda omwewo. Ndipo zikutsimikiziridwanso kuti Mtumiki Wopambana صلی اللہ علیہ واٰلہٖ وسلم anapemphera salah pamenepa.[1]

Masiku ano, munda umenewu unasinthidwa kukhala manda. Pakati pa manda pali mzikiti waung'ono wakalekale. Pabwalo la mzikiti pali chitsime chomwe sichili mmawonekedwe abwino. Wolemba mbiri akufotokoza kuti: "Nthawi iliyonse ndakwanitsa kulowamo, Ndimapezamo zinthu zomwe zagwiritsidwa ntchito pa maliro mu nzikiti umenewu!" Kunja kwa khoma la malire, kuli nzikiti wakamangidwe kachikale opanda denga omwe unamangidwa. Wofufuza ananena kuti nzikiti umenewu ulibe mbiri iliyonse yopambana, popeza nzikiti weniweni uli mkati mwa munda.

صَلُّوْا عَلَی الْحَبِیْب    صَلَّی اللہُ عَلٰی مُحَمَّد

[1] Jadhb al-Qulūb, tsamba. 127

## 11. Masjid Banī Qurayẓah

Mzikiti umenewu unali pakati pa Masjid Faḍīkh ndi Mashrabah Umm Ibrāhīm pafupi ndi Ḥarrah Sharqiyyah, pantunda wawutali ndithu kuchokera ku Masjid al-Shams kum'mawa. Panthawi imene ntundu wa Banū Qurayẓah unazunguliridwa, Mtumiki Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anasankha mzikiti umenewu kuti mapemphero achitikire m'menemo.[1] Malinga ndi nkhani ina, Masjid Banī Qurayẓah unamangidwa pamalo pomwe denga linakhonzedwa kuti Mtumiki wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم mu chaka cha 5 pambuyo pa nsamuko(627 AD) panthawi ya nkhondo ya Banū Qurayẓah. Malinga ndi nkhani ina, chapafupi panali nyumba ya mayi wina imene Mtumiki Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anapempheramo salah. Sayyidunā ʿUmar b. ʿAbd al-ʿAzīz رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anayipanga nyumba ija kukhala mbali ya nzikiti panthawi imene amkakulitsa mzikitiwo.[2]

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب     صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## 12. Masjid al-Nūr

Sayyidunā Usayd b. Ḥuḍayr ndi Sayyidunā ʿAbbād b. Bishr رَضِيَ اللّٰهُ عَنْهُمَا anapita kunyumba mochedwa kwambiri usiku pambuyo poti anakhala ndi Mtumiki Wopambana صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم.

---

[1] Fatḥ al-Bārī, buku. 8, tsamba. 106

[2] Jadhb al-Qulūb, tsamba. 126

Panthawi yomwe sanakwanitse kupeza njira chifukwa cha m'dima, ndodo ya Sayyidunā Usayd b. Ḥuḍayr رضی اللہ عنہ mwadzidzidzi, inayamba kuwala, ndipo onse awiri anapitiriza kuyenda mu kuwala kwa ndodo ija. Panthawi imene njira zawo zinasiyana, ndodo ya Sayyiduna ʿAbbād b. Bishr رضی اللہ عنہ inayamba kuwalanso nayo. Motero, onse awiri anakafika m'manyumba mwawo pogwiritsa ntchito kuwala komwe kumachokera mu ndodo zawo.[1]

Sayyidunā ʿUmar b. ʿAbd al- ʿAzīz رحمۃ اللہ علیہ anamanga Masjid al-Nūr pamalo omwe Masahaba awiriwa anasiyana, kumpoto chakum'mawa kwa Masjid al-Nabawī, kumbali ya manda a al-Baqīʿ kumene mtundu wa Bani ʿAbd al-Ashhal unkakhala.

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## 13. Masjid al-Fasḥ

Pali nzikiti wa wung'ono pansi pa Phiri la Uḥud cha ku Shiʿb al-Jirār. Wankhondo Wachichepere Wotchuka pa nkhondo ya Uḥud Sayyidunā Rāfiʿ رضی اللہ عنہ anafotokoza kuti Mtumiki Wopambana صلی اللہ علیہ والہ وسلم anapemphera salah zingapo mu nzikiti umenewu.[2] Malingana ndi al-Maṭarī, Mtumiki Wolemekezeka صلی اللہ علیہ والہ وسلم anapemphera salah ya Ẓuhr komanso salah ya

[1] Musnad Imam Aḥmad, buku. 4, tsamba. 277, hadith 12,407

[2] Tārīkh al-Madinah al-Munawwarah li Ibn Shabah, buku. 1, tsamba. 57



www.dawateislami.net

ʿAṣr pamenepa.[1] Olemba Mbiri ena ali ndi maganizo oti mabala amene Mtumiki wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anavulala pa nkhondo ya Uḥud anatsukidwa pamenepa. Choncho, unkatchedwa Masjid al-Ghasl. Kalekale, Ineyo [wolemba] عُفِيَ عَنْهُ ndinawona bwinja la nzikiti litazunguliridwa ndi waya waminga pa malo amenewa. Mwina umenewo unali nzikiti wa al-Fasḥ. Chimenechi ndi chikumbutso kutikumbutsa ife pa malo amene Mtumiki wathu Wopambana صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anapangirapo sajidah.

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## 14. Masjid Banī Ẓafar (kapena Masjid al-Baghlah)

Panali mtundu wotchedwa Banī Ẓafar, umene unali nthambi ya Aws. Anthu a mtundu umenewu ankakhala kudera limene lili cha kum'mawa kwa manda a al-Baqiʿ ku mbali ya Ḥarrah Sharqiyyah. Nzikiti wa Banī Ẓafar unali pamenepo. Umatchedwanso Masjid al-Baghlah. Pamene anakhala pa thanthwe pamenepo, Mtumiki wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ananvela kuwerenga kwa Quran Yolemekezeka kwa Sayyidunā ʿAbdullāh b. Masʿūd رَضِيَ اللهُ عَنْهُ ndipo analira kwambiri mpaka ndevu zake zodalitsika zinanyowa ndi misozi.[2]

[1] Wafāʾ al-Wafāʾ, buku. 2, tsamba. 848

[2] Al-Muʿjam al-Kabīr, buku. 19, tsamba. 243, hadith 546



www.dawateislami.net

Mwala umenewo unayikidwa mu nzikiti ngati chotsalira chopatulika. Omukonda Mtumiki صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ankayang'ana maso awo pa mwalawo. Olemba mbiri ena anafotokoza kuti azimayi opanda ana ankapanga ma du'a atakhala pa mwalapo, zimenezi zimapangitsa kuti adalitsidwe ndi ana.[1] Panalinso zikumbutso zina pamenepa, kuphatikizapo mwala umene unali ndi chizindikiro cha phazi la bulu wa Mtumiki, amene iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anakwera. Mwala wina uli ndi zizindikiro (zidindo) za chigongono komanso zala zodalitsika za Mtumiki صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم.[2]

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## 15. Masjid al-Māʾidah

Nzikiti wa al-Maʾidah unali pafupi ndi Nzikiti wa Banī Ẓafar. Zikukambidwa kuti unamangidwa pa malo amene Mtumiki Wopambana صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anasankha kuti *mubāhalah* ndi akhristu aku Najrān inachitikira. Komanso, ndi malo ake omwewa amene Sayyidunā Salmān al-Fārisī رَضِىَ اللهُ عَنْهُ anamumangira denga Mtumiki Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم pokankhira mitengo yamatabwa pansi ndi kumanga nsalu yake ku mitengoyo.

[1] Jadhb al-Qulūb, tsamba. 128

[2] Jadhb al-Qulūb, tsamba. 128



www.dawateislami.net

Mtumiki wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيۡهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anapita pamenepo pamodzi ndi akubanja ake. Malingana ndi mbiri yakale, ndi pamenepa pomwe chakudya chinafika pa mbale zokwana zisanu kuchokera kujannah chinatumizidwa kupita kwa Mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيۡهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndi akubanja ake. Choncho, umatchedwanso Nzikiti wa Mbale Zisanu. Pokumbukira zimenezi, omukonda Mtumiki anamanga zimphika pamenepa. Mu chaka cha 1400 pambuyo pa nsamuko, Ndinawona mabwinja a malo opatulikawa. Panalibepo zimphika. Komabe, ndi mitima yachisoni, kuyendera komanso kupeza madalitso kuchokera pa malo amenewa ndi chinthube chopambana kwa omukonda mtumiki. Komabe, ndizopambana kwambiri kudzimiza wekha mu chikondi cha Mtumiki Wopambana صَلَّى اللّٰهُ عَلَيۡهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم poyendera komanso kuwona malo amenewa.

صَلُّوۡا عَلَی الۡحَبِیۡب　　　صَلَّی اللّٰهُ عَلٰی مُحَمَّد

## 16. Masjid Banī Ḥarām

Sayyidunā ʿUmar b. ʿAbd al-ʿAzīz رَحۡمَةُ اللّٰهِ عَلَيۡه — omukonda Mtumiki wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيۡهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم weniweni — anamanga nzikiti umenewu pamene panali nyumba ya Sayyidunā Jābir b. ʿAbdullāh رَضِىَ اللّٰهُ عَنۡهُ. Pamenepa, zozizwitsa zitatu za Mtumiki Wopambana صَلَّى اللّٰهُ عَلَيۡهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم zinachitika:

1. Nyama ya mbuzi imodzi inakwanira chiwerengero cha masahaba عَلَيۡهِمُ الرِّضۡوَان chochuluka kwambiri amene anadya



www.dawateislami.net

mpaka kukhuta. (Malingana ndi nkhani imodzi, anali okwana 1500).

2. Mtumiki Wopambana صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anayika dzanja lake pa mafupa kenako anawerenga zina zake, zimene zinapangitsa mbuzi kuti ikhalenso ndi moyo.

3. Ana omwalira a Sayyidunā Jābir رَضِیَ اللهُ عَنْهُ anawuka kwa akufa ndi kupambana kwa du'a ya Mtumiki صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم wokondedwa.

(Tsatanetsane wa nkhani zolimbikitsa chikhulupiriro zitha kuwerengedwa pa tsamba 228-231 mu buku loyamba la *Faizan-e-Sunnat.*)

Mtumiki Wopambana صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anapempheranso Salah imodzi mu nyumba yodalitsikayi. Mzikiti opatulikawu ukupezeka pansi pa phiri la Salᶜ kudera lotchedwa Al-Sīh, limene lili kumanja kwa nsewu ochokera ku al-Masjid al-Nabawī kupita ku Khamsah Masājid. Mu chaka cha 1409 pambuyo pamsamuko, nzikiti wokongola unamangidwa pa maziko a nzikiti wakale, komano anthu opanga hajj ndi umrah a mayiko ena nthawi zambiri samawuwona chifukwa ndizovuta kupeza nzikiti umenewu mkatikati mwa malo okhala anthu ambiri wa.

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب        صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## 17. Masjid al-Shaykhayn

Popita kuchokera ku al-Masjid al-Nabawī kupita ku malo a mpumulo odalitsika a Sayyidunā Ḥamzah رَضِیَ اللهُ عَنْهُ, munthu atha kuwona nzikiti umenewu chapatali mbali ya kumanzere.

Zinthu zambiri zinachitika pamenepa, zina mwa izo ndizomwe zatchulidwa pansizi:

1. Akupita ku nkhondo ya Uḥud, Mtumiki صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم poyamba anayima pamenepa ndipo anakhala gawo lina la usiku pamenepa.
2. Mtumiki Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anapemphera salah imodzi kapena ziwiri pamenepa.
3. Pa malo omwewa, Mtumiki wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anavala chishango chake ndipo ananyamula zida zake.
4. Amenewa ndi malo amene kukonzekera kwa nkhondo kunawongoleredwa, ankhondo anasankhidwa, ndipo ana ambiri anabwenzedwa.
5. Pamalo omwewa, Sayyidunā Rāfiʿ رَضِیَ اللهُ عَنْهُ, amene anali mwana pa nthawiyi, anayima ndi zala zake ndicholinga chakuti awoneke wamkulu, ndipo Mtumiki woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anamupatsa chilolezo. Powona zimenezi, mwana wina wotchedwa Samurah b. Jundub رَضِیَ اللهُ عَنْهُ ananenetsa kuti ndi wamphanvu kuposa Rāfiʿ. Choncho,

kulimbana kunachitika pakati pa awiriwa, ndipo Samurah anawina; motero, anapeza chilolezo chopita nawo.

Nzikiti umenewu umatchedwa Masjid al-Shaykhayn chifukwa panali malinga awiri pamenepa. Linga limodzi linali la Myuda wokalamba wakhungu wam'muna, ndipo linga linalo linali la Myuda wokalamba wakhungu wamkazi. Mu chiyankhulo cha chiarabu, 'shaykh' amatanthawuza munthu wokalamba. Choncho, malo amenewa amatchedwa Shaykhayn chifukwa cha anthu awiri okalambawo. Nzikiti umenewu ulinso ndi mayina ena: (i) Masjid al-Dirʿ (ii) Masjid al-Badāˈiʿ (iii) Masjid ʿAnawī. Nzikiti umenewu unamangidwa kachikena mwamakono ndima Awqāf Aku Madinah ndipo unapatsidwa dzina loti Masjid al-Khayr.

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## 18.Masjid al-Mustarāḥ

Mzikiti umenewu ukupezeka m'mbali mwa nsewu popita ku phiri la Uḥud pa ntunda wawufupi kuchokera pa Masjid al-Shaykhayn. M'masiku oyambirira achisilamu, unkatchedwa Masjid Banī Ḥārithah monga fuko la Banī Ḥārithah (kuchokera ku mtundu wa Aws) linkakhala pamenepo. Malinga ndi nkhani, Sahaba wolemekezeka (al-Ḥārith b. Saʿīd b. ʿUbayd al-Ḥārithī رضی اللہ عنہ) ananena kuti Mtumiki



www.dawateislami.net

wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anapemphera salah mu nzikiti wa Banī Ḥārithah.[1]

Mtumiki Wopambana صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anapuma pamenepa kwakanthawi pamene ankabwerera kuchokera ku nkhondo ya Uḥud. Choncho, umatchedwa Masjid al-Mustarāḥ. Masiku ano, nzikiti wokongola unamangidwa pamenepa.

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## 19. Masjid al-Misbah kapena Masjid Banī Unayf

Moyang'anizana ndi Masjid Qubāʾ pali njira yokhala ndi anthu ambiri pafupi pake. Pantunda wawufupi chabe kuchokera ku مُسْتَوْدَعَاتُ الْغَسَّان, mkatikati mwa malo okhala anthu ambiri, muli zipupa za nzikiti opanda denga umene suli m'mawonekedwe abwino okhala ndi milu ya zinyalala mozungulira. Umenewu ndi nzikiti wa al-Muṣabbiḥ. (Allah Wamphanvu zonse akudziwa m'mene nzikitiwo uliri panopa.) Anthu a ntundu Banī Unayf ankakhala pamenepa. Ndi malo amenewa omwe Masahaba عَلَيْهِمُ الرِّضْوَان ankamudikira Mtumiki wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم kuti afike kuchokera ku Makkah. Pamapeto pake, zokhumba zawo zinakwaniritsidwa, ndipo Mtumiki Wopambana صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anasamukira ku Madinah. Awa ndi malo omwe Mtumiki wa

[1] Wafāʾ al-Wafāʾ, buku. 2, tsamba .865

Allah صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anapempherapo Salah ya Fajr yoyamba pambuyo pa nsamuko.

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## 20. Masjid Banī Zurayq

Atalowa chisilamu pa mwambo wa m'gwirizano oyamba umene unachitika pa malo otchedwa al-ʿAqabah, Sayyidunā Rāfiʿ b. Mālik al-Zuraqī رَضِیَ اللهُ عَنْهُ anamanga nzikiti umenewu ngakhale Mtumiki Wopambana صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم asanafike ku Madinah. Anthu okhulupirira ankapemphera pamenepo komanso kuwerenga gawo la Quran Yolemekezeka limene linali litavumbulutsidwa pa nthawi imeneyo ndipo linaphunzitsidwa kwa Sayyidunā Rāfiʿ b. Mālik al-Zuraqī رَضِیَ اللهُ عَنْهُ ndi Mtumiki Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم. Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم analowa mu nzikiti umenewu.[1]

Nzikiti wa Banī Zurayq unali penapake pakati pa Masjid al-Ghamāmah ndi bwalo lomwe lilipo panopa. Omukonda Mtumiki akuyenera kuyendera malo amenewa ndi chitsimikizo Chabwino, choncho adzapeza madalitso.

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

[1] Wafā' al-Wafā', buku. 2, tsamba. 857



www.dawateislami.net

## 21. Masjid Katībah

Sahaba oyamba wachi Anṣārī wa ku Madinah, Sayyiduna Rāfiʿ b. Mālik al-Zuraqī رَضِيَ اللهُ عَنْهُ, anaphedwa pa nkhondo ya Uḥud. Iye رَضِيَ اللهُ عَنْهُ anayikidwa m'nyumba mwake. Kenako, anthu akubanja kwake anamanga nzikiti pamalo a nyumba yake pamene malo ake a mpumulo anali pabwalo. Ana ake anayambitsa njira yawuzimu ya Sanūsī Sufi. Ma Ottoman anamanga nyumba zongoyembekezera zankhondo pafupi ndi nzikiti umenewu. Mu chiarabu amati, كَتِيْبَه amatanthawuza asilikali kapena magulu ankhondo. Choncho, derali linkatchedwa 'Katībah', ndipo nzikiti unadziwika ndi dzina loti Masjid al-Katībah. Nzikiti umenewu, ndi nsanja zake zakalekale, unalipo mpaka zaka zingapo isanafike nthawi yolemba izi. Salah inkapempheredwa kasanu patsiku.

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## 22. Masjid Banī Dīnār

Pambuyo pa nsamuko, Sayyidunā Abū Bakr al-Ṣiddīq رَضِيَ اللهُ عَنْهُ anakwatira nkazi ochokera ku banja la Banī Dīnār b. al-Najjār ku Madinah. Nthawi inayake, anamuyitana Mtumiki صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم kuti apite ku nyumba yake ndipo akapemphere Salah kumeneko. Pempho lake linavomerezedwa, ndipo Mtumiki صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anapitako ndipo anapemphera salah.[1]

[1] Wafāʾ al-Wafā, buku. 2, tsamba. 866



www.dawateislami.net

Pokumbukira zimenezi, Sayyidunā ʿUmar b. ʿAbd al-ʿAzīz رَحْمَةُاللّٰهِعَلَيْه anamanga Masjid Banī Dīnār. Kenako, dera linka khalidwa ndi anthu ochapa zovala. Zovala zinkachapidwa pamenepo, ndipo malowa ankatchedwa ndi dzina loti Ghassālīn, zimene zinapangitsa kuti nzikiti uzichedwa Masjid al-Ghassālīn. Masiku ano, nzikiti umenewu umatchedwa Masjid al-Mughaysalah.

Malo atsopano a nzikiti umenewu ndi pafupifupi theka la kilomita nkati mwa malo okhala kuseli kwa Madrasah ʿAskariyyah, Maḥallat al-Māliḥah. Nzikiti wawukulu umene uli ndi zipangizo zatsopano unamangidwa pafupi ndi nzikiti wopatulika wakalewu, kuchotsa chidwi cha anthu pa nzikiti wakalewo; kupambana kwake kwenikweni kukuyiwalika.

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب    صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## 23. Masjid al-Mīnāratayn

Sayyidunā Ḥarām b. Saʿd Bin Muḥayyiṣah رَضِىَ اللهُ عَنْهُ anafotokoza kuti Mtumiki Wopambana صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anapemphera salah pa malo amenewa.[1]

Pokumbukira izi, anthu omukonda Mtumiki anamanga nzikiti wa al-Mīnāratayn pamalo omwewa. Ngati mukupita ku chigwa cha ʿAqīq kuchokera ku al-Masjid al-Nabawī Potsatira Shāriʿ

[1] Wafāʾ al-Wafā, buku. 2, tsamba. 878-879



www.dawateislami.net

ʿAnbariyyah (kalekale imatchedwa Shāriʿ Makkah), pambuyo poti mwayenda pafupifupi theka la kilomita, mudzawona malo omwetsera mafuta. Kenako chapatsogolo pang'ono pali malo otseguka chakumanja kumene nzikiti wawukulu kwambiri unamangidwa. Nzikiti umenewu umatchedwa Masjid al-Mīnāratayn.

## Mbuzi yakufa

Mtumiki wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ankadutsa dera la Masjid al-Mīnāratayn pamodzi ndi omutsatira ake عَلَيْهِمُ الرِّضْوَان. Ali munjira, Mtumiki wa Allah صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anawona mbuzi yakufa ndipo fungo loyipa limatuluka kuchokera ku mbuziyo. Anatseka Masahaba عَلَيْهِمُ الرِّضْوَان mphuno zawo pogwiritsa ntchito nsalu. Mtumiki Wopambana صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anafunsa kuti, "Ndizinthu ziti zomwe mukuwona kuti mbuzi iyi ingakhudze mwini wake?"

Anayankha, "E Mtumiki wa Allah صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم, ndi zinthu ziti zomwe zingakhudze mwini wake?"

Mtumiki Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anayankha, "Dziko ili ndi lotsika kwambiri kwa Allah Wamphanvu zonse kuposa mbuziyi kwa mwini wake."[1]

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

[1] Wafāʾ al-Wafā, buku. 2, tsamba. 878

## 24. Masjid al-Jumuʿah

Nzikiti umenewu ukupezeka mbali yakumanja ya nsewu tikamayenda kuchokera ku Masjid Qubāʾ kupita ku al-Masjid al-Nabawī. Pa nthawi ya nsamuko, pambuyo poyendera Qubāʾ, Mtumiki Wopambana صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndi omutsatira ake عَلَيْهِمُ الرِّضْوَان ananyamuka wa ku Madinah. Panthawi yomwe anafika dera la Banī Sālim, anthu akumeneko anawapempha kuti ayime pamenepo kwa kanthawi. Pempho lawo linayankhidwa. Panthawiyi, nthawi ya Salah ya Jumuʿah inayamba, choncho Mtumiki Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndi Masahaba ake عَلَيْهِمُ الرِّضْوَان anapemphera salah ya Jumuʿah yoyamba pa malo amenewa komanso pa gulu. Nzikiti unamangidwa pa malo amene Salah inapempheredwa.

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## 25. Masjid al-Muʿarrās

Nzikiti umenewu unali molunjika mbali ya ku Qiblah pa Dhū al-Ḥulayfah, *mīqāt* ya anthu okhala ku Madinah. Apa ndipamene Mtumiki wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anakhalapo usiku komanso kupuma pambuyo poti iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم wabwerera kuchokera ku Makkah. Nzikiti umenewu si umawonekanso palibepo.

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد



www.dawateislami.net

## 26. Masjid Dhū al-Ḥulayfah

Nzikiti umenewu ukupezeka kum'mwera cha kum'mawa kwa al-Masjid al-Nabawī pa ntunda wa pafupifupi ma kilomita 9. Masiku ano, malo amenewa amatchedwa Bīr ʿAlī kapena Abyār ʿAlī, ndipo ndi mīqāt ya anthu okhala ku Madinah. Dzina lakale la Masjid Dhū al-Ḥulayfah ndi Masjid al-Shajarah. Sayyidunā ʿAbdullāh b. ʿUmar رَضِيَ اللّٰهُ عَنْهُمَا anafotokoza kuti Mtumiki Wopambana صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ankatuluka mu Madinah pogwiritsa njira ya al-Shajarah ndipo ankalowa mu Madinah potenga njira ya al-Muʿarras. Akamapita ku Makkah, iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ankapemphera salah mu nzikiti wa al-Shajarah, ndipo akamabwelera, iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ankapemphera salah pa Dhū al-Ḥulayfah nkatikati mwa chigwa. Mtumiki صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ankakhala pamenepo usiku wonse mpaka mamawa.[1]

Sayyidunā ʿAbdullāh b. ʿUmar رَضِيَ اللّٰهُ عَنْهُمَا anafotokoza kuti Mtumiki Wopambana صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anakhala usiku pa Dhū al-Ḥulayfah ndipo anapemphera salah pa nzikiti wa pamenepo.[2]

Pamene Mtumiki wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ananyamuka ulendo okapanga Ḥajjat al-Wadāʿ ndipo atafika pa Dhū al-Ḥulayfah, iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anapemphera ma rakah a salah pamenepo mu

[1] Ṣaḥīḥ al-Bukhari, buku. 1, tsamba. 516, hadith 1,533

[2] Ṣaḥīḥ Muslim, tsamba. 607, Hadith 1188

nzikiti.[1] Panopa, nzikiti wokongola otchedwa Masjid Dhū al-Ḥulayfah unamangidwa pamenepo.

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب          صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## 27. Masjid al-Qiblatayn

Nzikiti umenewu uli pafupi ndi chipululu cha al-ʿArṣah mu chigwa chaʿAqīq' pa al-Ḥarrat al-Wabarah (al-Ḥarrat al-Gharbiyyah). Mizikiti isanu ilinso pafupi. Ngati mukuyenda kuchokera ku Madinah, Biˈr al-Rūmah (chitsime cha Sayyidunā ʿUthmān رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ) chili chakumanja kwa nzikiti umenewu. Mtumiki Wopambana صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anapemphera salah ya Ẓuhr pamenepa. Poyamba unkatchedwa Masjid Banī Sulaym chifukwa ntundu wa Banū Sulaym unkakhala pa malo amenewa. Loweruka pa 15 Rajab mu chaka cha chiwiri pambuyo pa nsamuko (Januwale 624 CE) —miyezi yokwana 16 pambuyo pa nsamuko —Mtumiki Wopambana صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم atangomaliza ma rakah awiri okha a salah ya Ẓuhr ndipamene lamulo losintha Qiblah linaperekedwa. Ma rakah awiri otsalira anapemphera atayang'ana ku Kaaba. Choncho, nzikiti unatchuka ndi dzina loti Masjid al-Qiblatayn (nzikiti wa ma Qiblah awiri).

Pokumbukira izi, omukonda Mtumiki anayika chizindikiro cha Qiblah pa khoma lolunjika ku  Bayt al-Muqaddas ndipo

[1] Tārīkh al-Madinah al-Munawwarah, tsamba. 501-502

analembapo ndime yodalitsika yokhudza kusintha kwa Qiblah. Anthu ochita Hajj komanso Umrah anali akugwira chizindikiro chimenechi ndi cholinga chopeza madalitso. Khoma limenero panopa linachotsedwa, ndipo chithunzi cha mphasa yopempherera chinayikidwa pa khoma la khomo lalikulu, kusonyeza mbali ya Qiblah yoyamba.



www.dawateislami.net

الحمد لله رب العلمين والصلوة والسلام على سيد المرسلين اما بعد فاعوذ بالله من الشيطن الرجيم بسم الله الرحمن الرحيم

## Kukhala msilamu woopa mulungu ndi wopemphera Salah

Khalani usiku onse mu ijtima ya Dawat-e-Islam yolimbikitsa sunna yomwe imachitika lachinayi sabata iliyonse pambuyo pa salat-ul-maghrib m'dera lanu, chifukwa chomusangalatsa Allah عزوجل, ndi zolinga zabwino. Kuti muphunzire ma Sunnah, chipangeni kukhala chizolowezi chanu choyenda ndi Madani Qafilah masiku atatu mwezi uliwonse pamodzi ndi odzipereka a Rasool, kumalizitsa kulemba mkabuku ka Madani In'amaat tsiku lilonse kuchita fikr-e-Madina ndikukapereka kwa m'bale wachisilamu woyenera yemwe ali ndi udindo mdera lanu tsiku loyamba la mwezi uliwonse wa Madani.

**Cholinga changa cha madani**

Ndiyenera kuyesetsa kudzikonza ndekha ndi anthu apadziko lonse lapansi, ان شاء الله. Ndicholinga choti tidzisinthe tokha, tiyenera kuchitapo kanthu pa Madani In'amaat ndikuyesetsa kusintha anthu a dziko lonse lapansi, tiyenera kuyenda ndi Madani Qafilah ان شاء الله.




Aalami Madani Markaz, Faizan-e-Madinah, Mahallah Saudagaran
Purani Sabzi Mandi, Bab-ul-Madinah, Karachi, Pakistan
UAN: +92 21 111 25 26 92 | Ext: 7213
Web: www.dawateislami.net | E-mail: translation@dawateislami.net